



NJIRA YA KUYERETSERA ZOVALA



Shaykh-e-Tareeqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat
Muyassidul-Usul wa Dawa-e-Ilahi,
Allamah Maulana Abu Bilal

MUHAMMAD ILYAS
Attar Qadiri Razavi رحمۃ اللہ علیہ

کپڑے پاک کرنے کا طریقہ (مع نجاستوں کا بیان)

Kapṛay Pāk Kernay kā Ṭarīqah (ma' Najāsaton kā Bayān)

NJIRA

YOYERETSERAZOVALA

(komanso Kufotokozera Za Zonyansa)

Kabukuka kanalembedwa ndi Shaykh-e-Ṭarīqat Amīr-e-Aḥl-e-Sunnat, amene anayambitsa Dawat-e-Islami ‘Allāmaḥ Maulānā Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ **al-ʿAlāyih** mu chiyankhulo cha Urdu. **Nthambi Yomasulira** yamasulira kabukuka mu Chichewa. Ngati mutapeza cholakwika chilichonse pomasulira kapena pa kapangidwe, chonde dziwitsani nthambi yomasulira pa keyala kapena imelo ili m’mutsiyi ndi cholinga chopeza malipiro [Ṣawāb].

Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)

Alami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

Foni: ☐ +92-21-34921389 to 91

Imelo: ☐ translation@dawateislami.net

Tchatl Chomasulira

ء	A/a	ڑ	Ř/ř	ل	L/l
ا	A/a	ز	Z/z	م	M/m
ب	B/b	ژ	X/x	ن	N/n
پ	P/p	س	S/s	و	V/v,
ت	T/t	ش	Sh/sh		W/w
ٹ	Ṭ/ṭ	ص	Ṣ/ṣ	ۀ / ه / هـ	Ĥ/ĥ
ث	Ṣ/ṣ	ض	Ḍ/ḍ	ی	Y/y
ج	J/j	ط	Ṭ/ṭ	ے	Y/y
چ	Ch	ظ	Ẓ/ẓ	َ	A/a
ح	H/h	ع	‘	ُ	U/u
خ	Kh/kh	غ	Gh/gh	ِ	I/i
د	D/d	ف	F/f	و مدہ	Ū/ū
ڈ	Ḍ/ḍ	ق	Q/q	ی مدہ	Ī/ī
ذ	Ẓ/ẓ	ك	K/k	ا مدہ	Ā/ā
ر	R/r	گ	G/g		

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ
الرَّحِيمِ

Du'ā Powerenga Buku

Werengani Du'a (pempho) musanawerenge buku
lachipembedzo kapena musanayambe phunziro
lachisilamu; mudzakumbukira china chilichonse
mwaphunzira, إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ:

اللَّهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْإِكْرَامِ

Kumasulira

Yā Allah عَزَّوَجَلَّ! Titsegulireni makomo a maphunziro
komanso a luntha ndipo tichitireni chisoni! E inu omwe muli
wolemekezeka kwambiri komanso aulemerero!

(Al-Mustaṭ raf, buku. 1, tsamba. 40)

Chidziwitso: Werengani Ṣalāt-ʿAlan-Nabī ﷺ kamodzi
musanayambe komanso kumapeto kwa Du'ā.

M'NDANDANDA WA ZOPEZEKAMO

NJIRA YOYERETSERA ZOVALA	1
Ubwino wa Ṣalāt-'Alan-Nabī ﷺ	1
Mitundu ya nyatsi	1
Najāsat-e-Ghalīẓah (nyatsi yayikulu)	1
Nkodzo wa makanda oyamwa siwoyera	4
Lamulo pa Najāsat-e-Khafīfah	7
Lamulo pa chakudya chogayidwa pang'ono	7
Lamulo lokhuza ndulu	7
Masanzi a nyama	8
Nkaka wa nyama za Ḥarām	13
Ndowe za mbewa	13
Madzi anvula ongoyima m'misewu	15
Madontho a madzi owazidwa munsewu	16
Nanga ngati galu wayika mulomo mu mphika	17
Zotuluka ku chiwalo chankodzo cha munthu wamkazi	19
Nyama yovunda	20
Botolo limene nkati mwake muli magari	20
Madzi ochokera nkamwa mwa Ntembo	20

Chidutswa cha khungu la munthu	21
Tingayeretse bwanji nyama komanso chikopa cha nyama ya Ḥarām?	22
Njira yoyeretsera zovala mu makina ochapira	29
Njira yoyeretsera zovala pa mpope	29
Kapeti yokuda ingayeretsedwe bwanji?	30
Tingayeretse bwanji manja amene apakidwa ndi henna onyatsa?	30
Kuchapa chovala chodetsedwa ndi mafuta	31
Ngati gawo lochepa la chovala lakhala lokuda...	31
Malamulo 6 a kuyeretsa zovala zimene zadetsedwa ndi umuna	32
Ndi nthawi yake iti imene ndi Wājib kumuwuza munthu zokhudza zovala zake kuti ndi zakuda?	33
Njira yoyeretsera ubweya wa thonje	34
Njira yoyeretsera galasi	35
Njira yoyeretsera nsapato	35
Majuzi ogwiritsidwa ntchito ndi zina zambiri za anthu oti si-Asilamu	36

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ
الرَّحِيمِ

NJIRA YOYERETSERAZOVALA

(Komanso Kufotokozera za Zonyansa)

Ubwino wa Ṣalāt-‘Alan-Nabī ﷺ

Mtumiki wa anthu, Mtendere wa mitima yathu ndi malingaliro athu, owolowa manja kwambiri ndi okoma mtima صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati: ‘Munthu amene angandiwerengere ine Ṣalāt (kundifunira zabwino) ka 100, Allah عَزَّوَجَلَّ amamulemba pakati pa maso ake awiri kuti iye ndi mfulu kuchokera ku chinyengo komanso moto wa gahena, ndipo Iye عَزَّوَجَلَّ adzamuyika iye pamodzi ndi anthu amene anafera mu njira ya Allah pa Tsiku la Chiweruzo.’

(*Majma’-uz-Zawāid, buku. 10, tsamba. 253, H adīṣ 17298*)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Mitundu ya nyatsi

Pali mitundu iwiri ya nyatsi:

1. Najāsāt-e-Ghalīẓah (nyatsi yayikulu)
2. Najāsāt-e-Khafifāh (nyatsi yopepuka)

(*Fatāwā Qaḍī Khān, buku. 1, tsamba. 10*)

Najāsāt-e-Ghalīẓah (nyatsi yayikulu)

1. Chilichonse chimene chimatuluka kuchokera m’thupi la munthu, ndipo chimapangitsa Ghusl kapena Wuḍū

kukhala Wājib ndi Najāsāt-e-Ghalīẓah – mwachitsanzo, ndowe, nkodzo, magari oyenda, mafinya, kusanza kodzadza nkamwa, kutaya magari a msambo/kutaya magari pambuyo pobereka, umuna, Maẓī, Waḍī¹. (*Fatāwā ‘Ālamgīrī, buku. 1, tsamba. 46*)

2. Magari amene sanatuluke kapena sanayendelere kuchokera pachilonda ndi oyera. (*Fatāwā Razawīyāh (zatchulidwa), buku. 1, tsamba. 280*)
3. Madzi otuluka mu diso lopweteka ndi Najāsāt-e-Ghalīẓah. Chimodzimodzi, madzi otuluka mu mchombo kapena nsonga ya mawere chifukwa cha kupweteka ndi Najāsāt-e-Ghalīẓah. (*ibid, buku. 1, tsamba. 269–270*)
4. Magari oyenda a nyama iliyonse ya pamtunda komanso nyama ndi mafuta a nyama yokufa yokha ndi Najāsāt-e-Ghalīẓah. (Nyama yokufa yokha ndi nyama imene imakhala ndi magari oyenda ndipo yafa mopanda kuphedwa kovomerezeka ndi Sharī’ah. Komanso, nyama imene yaphedwa ndi munthu wopembedza-moto, wopembedza-mafano kapena munthu wampatuko wachipembedzo ndi nyamanso yakufa yokha ngakhale munthu amene wapha nyama ya Ḥalāl monga mbuzi ndi zina zambiri powerenga بِسْمِ اللَّهِ أَكْبَرُ. Nyama komanso chikopa cha nyama imeneyi zimakhala zosayera. Komabe, ngati Msilamu wapha

¹ Onani matanthawuzo Maẓī ndi Waḍī mu gawo lachiwiri la buku loyamba la *Bahār-e-Sharī’at* (Urdu), lotsindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madīnah.

[Zolembe za womasulira]

ngakhale nyama ya Ḥarām malingana ndi njira ya Shar’īa, nyama yake imakhala yoyera koma kudya nyama imeneyi ndi Ḥarām. Lamulo limeneli silimagwira ntchito pa nkhumba imene ndi Najis-ul-‘Ayn mukunena kwina imene singayeretsedwe mwanjira ina iliyonse.)

5. Ndowe ndi nkodzo za nyama za Ḥarām zokhala ndi miyendo inayi monga galu, mkango, nkhandwe, mphaka, khoswe, bulu, nyulu, njovu ndi nkhumba; komanso ndowe za kavalo; komanso
6. Ndowe za nyama ya Ḥalāl iliyonse yokhala ndi miyendo inayi monga ng’ombe, njati, mbuzi, ngamira;
7. Zitosi za mbalame zomwe sizingawuluke m’mwamba kwambiri monga nkuku ndi bakha — kaya mbalame ndi yaying’ono kapena yayikulu;
8. Mtundu uliwonse wa mowa komanso chakudya choledzeretsa;
9. Ndowe komanso nkodzo wa njoka;
10. Nyama ya njoka zakutchire komanso achule zimene zili ndi magazi oyenda ngakhale zitaphedwa mwandondomeko. Chimodzimodzi zikopa za nyama zimenezi ngakhale zitawumitsidwa zikopazo;
11. Nyama, mafupa komanso ubweya wa nkhumba ngakhale itazingidwa kapena kuphedwa mwadongotsolo. Zonsezi ndi Najāsāt-e-Ghalīzāh. (*Bahār-e-Sharī’ at, buku. 2, tsamba. 112-113*)

12. Magazi a buluzi komanso bilimakhwe ndi Najāsāt-e-Ghalīzāh. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 113*)
13. Zotuluka ku chitamba cha njovu komanso malovu a mkango, galu, kambuku ndi nyama zina (zokhala ndi miyendo inayi) zolusa ndi Najāsāt-e-Ghalīzāh. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 113*)

Nkodzo wa makanda oyamwa siwoyera

Pali maganizo odziwika amene ndi olakwika onena kuti nkodzo wa makanda ndi oyera kapena kunena kuti siwonyatsa chifukwa samadya chakudya chilichonse. Zimenezi ndi zolakwika ndithu. Nkodzo komanso ndowe ngakhale za makanda oyamwa ndi Najāsāt-e-Ghalīzāh. Chimodzimodzi, ngati khanda loyamwa lasanza mkaka odzadza kukamwa, ndi Najāsāt-e-Ghalīzāh nso.

(*Zatengedwa kuchokera mu: Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 112*)

Lamulo pa Najāsāt-e-Ghalīzāh

Lamulo pa 'Najāsāt-e-Ghalīzāh' ndilakuti ngati yadetsa thupi kapena mbali ya chovala mu kuchuluka kumene kwaposa kukula kwa dirham, ndi Farḍ kuyiyeretsa. Ngati Ṣalāh yapempheredwa popanda kuyiyeretsa, Ṣalāh sidzatheka. Kupemphera Ṣalāh ukudziwa kuti uli chonchi (utadetsedwa ndi najāsāt-e-ghalīzāh) ndi tchimo lalikulu. Komanso, ngati Ṣalāh yapempheredwa uli chonchi poyitenga Ṣalāh ngati yopanda phindu, ndiye kuti ndi Kufr (kukanira).

Ngati Najāsāt-e-Ghalīzāh yadetsa thupi kapena mbali ya chovala mofanana ndi kukula kwa dirham, ndiye ndi Wājib

kuyiyeretsa. Ngati Ṣalāh yapempheredwa mopanda kuyeretsa thupi kapena chovala, Ṣalāh idzakhala Makrūh Taḥrīmī ndipo idzakhala Wājib Ṣalāh imeneyo kuyibwerezanso pambuyo poyeretsa chovala kapena thupi. Kupemphera Ṣalāh mwadala mopanda kuyeretsa Najāsāt-e-Ghalīzāh ndi tchimo.

Ngati Najāsāt-e-Ghalīzāh yadetsa thupi kapena mbali ya chovala ndipo ndiyochepera kuchuluka kwa dirham, ndi Sunnah kuyiyeretsa. Ngati Ṣalāh yapempheredwa mopanda kuyeretsa najāsāt-e-ghalīzāh , Ṣalāh idzakhala yatheka koma mosemphana ndi Sunnah. Ndi zopambana kubwereza Ṣalāh imeneyo.

(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 111)

Kufotokoza za kukula kwa dirham

Uku ndi kufotokoza zimene zikutanthawuza akamati Najāsāt-e-Ghalīzāh ndiyambiri, yochepa kapena yofanana ndi kukula kwa dirham.

Ngati Najāsāt-e-Ghalīzāh ndi yolimba ngati chimbudzi, ndowe ndi zina zambiri., dirham imodzi ikutanthawuza kuti kuchuluka kofanana ngati 4.50 galamu (kunena kwina.magalamu okwana 4.374) mu kulemera. Choncho, Najāsāt-e-Ghalīzāh yolimba kukhala yayikulu kapena yochepa kuposera dirham imodzi zikutanthawuza kuti Najāsāt-e-Ghalīzāh ndi yambiri kuposera 4.50 galamu kapena ndiyochepera 4.50 galamu mu kulemera. Ngati Najāsāt-e-Ghalīzāh ndi yopepuka ngati nkodzo ndi zina zambiri., dirham imodzi zikutanthawuza gawo linalake lomwe lingadziwike motere. Ikani dzanja ndipo

litambasuleni, kenako thirani madzi pang'onopan'ono mpaka madzi asatsalire mkati mwa dzanja. Tsopano gawo la kufalikira kwa madzi amenewa limatanthawuza dirham. *(Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 111)*

Ngati Najāsāt-e-Ghalīzāh yadetsa magawo osiyanasiyana a thupi kapena a chovala, ndipo palibe gawo limene ladetsedwa ndi kukula kofanana ndi dirham imodzi komano kuphatikiza magawo onse akukwana dirham imodzi (kunena kwina, kuchuluka kwa nyatsi kuchokera m'zigawo zonse kukukwana dirham imodzi), ndiyeno kuchuluka kudzatengedwa ngati dirham imodzi. Ndipo ngati kuchuluka kuli koposera dirham imodzi kudzatengedwa ngati kwaposa dirham imodzi. Pa nkhaninso ya Najāsāt-e-Khafīfah, lamulo lomweli lidzagwiritsidwa ntchito potengera kuchuluka konse. *(Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 115)*

Najāsāt-e-Khafīfah (nyatsi yo pepuka)

Najāsāt-e-Khafīfah zikuphatikizanso:

- C Nkodzo wa nyama zimene nyama yake ndi Ḥalāl (chitsanzo. ng'ombe, ng'ombe yothena, njati, mbuzi, ngamira ndi zina zambiri.) komanso nkodzo wa kavalo
- C Zitosi za mbalame zomwe nyama yake ndi Ḥarām, kaya zimapha ndi kudya nyama zina kapena ayi (chitsanzo. khwangwala, mphamba, ntundu wina wa kantema, kantema ndi zina zambiri.)

(Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 113)

Lamulo pa Najāsat-e-Khafīfah

Lamulo pa Najāsat-e-Khafīfah ndi lakuti ngati yadetsa gawo la thupi kapena chovala mu kuchuluka kumene kochepera 1/4 ya gawo limeneli, imakhululukidwa. Mwachitsanzo, ngati manja a chovala adetsedwa kapena dzanja lenireni ladetsedwa mu kuchuluka komwe kwa chepera 1/4 ya manja a chovala kapena dzanja lenireni, imakhululukidwa, kutanthawuza kuti Ṣalāh yopempheredwa uli chonchi imakhala yatheka. Komabe, ngati gawo lonse la 1/4 ladetsedwa ndi najāsat-e-khafīfah, Ṣalāh sidzatheka mpakana utadziyeretsa. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 111*)

Lamulo pa chakudya chogayidwa pang'ono

Lamulo pa chakudya chogayidwa pang'ono cha nyama iliyonse ya miyendo inayi ndilofanana ndi lamulo la pa ndowe zake. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 113; Durr-e-Mukhtār, buku. 1, tsamba. 620*)

Zochita za nyama zobwedzeretsa chakudya chomezedwa kale nkamwa ndikuchitafuna kachikenanso kumatchedwa chakudya chogayidwa pang'ono. Ng'ombe ndi ngamira zimakhala zikutafunabe, kupangitsa malovu a thovu kugwa pakamwa pa ng'ombe ndi ngamira. Malovu a thovu ndi zina zambiri. kuchucha pakamwa pa (ng'ombe, ngamira) chifukwa chakutafuna chakudya chogayidwa pang'ono ndi Najāsat-e-Ghalīzāh.

Lamulo lokhuza ndulu

Lamulo lokhuza ndulu ya nyama ina iliyonse ndi lofanana ndi lamulo la nkodzo wake. Ndulu ya nyama ya Ḥarām ndi

Najāsat-e-Ghalīẓaḥ pamene ndulu ya nyama ya Ḥalāl ndi Najāsāt-e-Khafīfaḥ. (*Durr-e-Mukhtār, buku. 1, tsamba. 620; Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 113*)

Masanzi a nyama

Lamulo lokhuza masanzi a nyama iliyonse ndi lofanana ndi lamulo la ndowe zake kunena kwina, nyama zimene chitosi chake ndichoyera monga mpheta kapena nkhunda, masanzi akenso ndi woyera; ndipo nyama zimene chitosi chake ndi Najāsāt-e-Khafīfaḥ monga kantema kapena khwangwala, masanzi akenso ndi Najāsāt-e-Khafīfaḥ. Chimodzimodzi, nyama zimene chitosi chake ndi Najāsāt-e-Ghalīẓaḥ monga nkhuku kapena bakha, masanzi akenso ndi Najāsāt-e-Ghalīẓaḥ. Masanzi pamenepa zikutanthawuza chakudya kapena madzi amene abwerera kuchokera m'mimba.

Nyama imene ndowe zake ndi nyatsi kapena zosayera, m'mimba mwake ndi gwero la nyatsi kapena kusayera. Chilichonse chingabwerere kuchokera m'mimba m'menemu, chidzakhala chonyansa pachokha kapena chosakanikirana ndi zonyansa. Mwina mulimonse, chidzakhala chili ndi zonyansa monga ndowe – Khafīfaḥ mu Khafīfaḥ komanso Ghalīẓaḥ mu Ghalīẓaḥ. Komabe, lamulo limeneli silimagwira pa chinthu chimene chabwerera chisanafike m'mimba. Mwachitsanzo, panthawi yokumwa madzi ngati nkhuku yayatsamwa, ndipo madzi atuluka asanafike m'mimba, choncho lamulo lokhuza chitosi cha nkhuku silidzagwira ntchito pa madzi amenewa. لَاَئِهٖ مَا اسْتَحَالَ إِلَى نَجَاسَةٍ وَلَا لَاقِي مَحَلَّهَا (kumasulira kuti, *chifukwa chakuti madzi amenewa sanasakanikirane ndi zonyatsa komanso madziwa sanakagunde gwero la zonyatsa.*) M'malo mwake, lamulo lokhuza madzi amenewa lidzakhala chimodzimodzi

ngati lamulo la zinthu zotsalira zimene chinyama chasiya chifukwa madzi amenewa abwerera kuchokera nkamwa mwake. Zinthu zotsalira zimene nyama yasiya zitha kukhala Najāsat-e-Ghalīzāh kapena Najāsat-e-Khafīfah kapena zokayikitsa kapena Makrūh kapenanso zoyera. Lamulo lomweli langati lazokhuza zinthu zotsalira lidzagwiranso pa chimene chabwerera kuchokera nkamwa chisanafike m'mimba ya nyama imeneyo. Zotsalira zimene nkhuku yoyendayenda yasiya ndi Makrūh choncho madzi atchulidwa m'mwambamu adzakhalsanso Makrūh. Ndipo ngati madzi abwerera pambuyo pofika m'mimba ndiye madziwa adzakhala Najāsat-e-Ghalīzāh. *(Fatāwā Razawīyyah (zatengedwa), buku. 4, tsamba. 390-391)*

Ngati nyatsi yagwera mu nkaka kapena madzi...

Malamulo atchulidwa mosiyana pa Najāsat-e-Ghalīzāh ndi Khafīfah amagwira ntchito pa nthawi imene nyatsi yadetsa thupi kapena chovala basi. Koma ngati nyatsi, kaya Najāsat-e-Ghalīzāh kapena Najāsat-e-Khafīfah, yagwera mu Chinthu chamadzimidzi ngati nkaka kapena madzi, nkaka umenewo kapena madzi amenewo ziwiri zonse zidzakhala zodetsedwa ngakhale nyatsi itakhala dontho limodzi. Ngati Najāsat-e-Khafīfah yasakanikirana ndi Najāsat-e-Ghalīzāh zonse zidzakhala Najāsat-e-Ghalīzāh.

(Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 112-113)

Momwe mungayeretsere khoma, nthaka, ntengo ndi zina zambiri ?

1. Ngati gawo la nthaka lodetsedwa lawuma, kupangitsa zizindikiro za nyatsi monga ntundu wake ndi fungo lake

kusawoneka zikatero nthaka yo imakhala yoyera posatengera kuti nyatsi yawuma chifukwa cha mphepo, dzuwa kapena moto. Choncho, Ṣalāh itha kupempheredwa pa nthaka imeneyo komano Tayammum singachitike ndi dothi la pa nthaka imeneyi.

2. Mtengo, udzu, khoma ndi njerwa imene yakhazikika pa nthaka zonse zimayera zikawuma (ngati zizindikiro monga ntundu ndi fungo za nyatsi sizikuwoneka). Ngati njerwa siyokhazikika pansi ndiye njerwa sidzakhala yoyera pongowuma chabe koma zidzakhala zoyenera kuyitsuka. Chimodzimodzi, ngati ntengo kapena udzu zadulidwa nyatsi isanawume, ndiyeno ndi zoyenera kutsuka ntengo kapena udzu kuti ziyeretsedwe. *(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 123)*
3. Mwala umene siwungachotsedwe kuchokera pa nthaka udzakhala wayeretsedwa panthawi imene wawuma komanso zizindikiro za nyatsi palibepo; apo ayi ndi zoyenera kutsuka mwalawo. *(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 123)*
4. Ngati china chake chimene chalumikizana ndi nthaka chakhala chodetsedwa ndipo chachotsedwa mu nthaka pambuyo poti chawuma, (kupangitsa zizindikiro za nyatsi kusawoneka), chidzakhallabe choyera. *(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 124)*
5. Ngati chinthu chayeretsedwa chifukwa cha kusisitidwa kapena kuwumitsidwa chapezeka kuti chanyowa nthawi ina, pamenepa sichidzakhala chodetsedwa. *(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 124)*

Mwachitsanzo, gawo la nthaka lakhala lodetsedwa chifukwa cha kukodzapo. Kenako, lawuma ndipo zizindikiro za nyatsi sizikuw onekanso, choncho nthaka imakhala kuti yayera. Tsopano ngati nthaka imeneyo yanyowa kachikenanso ndi madzi oyera aliwonse, sidzakhala yodetsedwa.

Njira yoyeretsera nthaka yodetsedwa ndi magari

Ngati mwana kapena munthu wankulu wakodza kapena kupanga chimbudzi pa nthaka kapena magari kapena mafinya otuluka kuchokera pa chilonda kapena magari otuluka pamene nyama ikuzingidwa, agwera pa nthaka ndipo apukutidwa ndi nsalu iliyonse ndi zina zambiri popanda kugwiritsa ntchito madzi, gawo la nthaka imeneyo idzakhala yayera pambuyo poti nthakayo yawuma ndipo zizindikiro za nyatsi sizikuwoneka. Şalâh ithanso kupempheredwa pamenepo.

Gawo la nthaka lopakidwa ndi ndowe

Şalâh singapempheredwe mopanda kuyika chinthu pa gawo la nthaka lopakidwa ndi ndowe ngakhale nthakayo yawuma. Komabe, ngati Şalâh yapempheredwa pa nsalu yolimba imene yayalidwa pa nthaka yopakidwa ndi ndowe ndipo nthakayo ndiyowuma, ndiyeno Şalâh idzakhala yatheka.
(Bafîr-e-Sharî' at, buku. 2, tsamba. 126)

Mbalame zimene ndowe zake ndi zoyera

1. Nkodzo komanso chitosi za mleme² zonse ziwiri ndi zoyera. (*Durr-e-Mukhtār, Rad-dul-Muḥ tār, buku. 1, tsamba. 574; Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 113*)
2. Zitosi za mbalame za Ḥalāl zowuluka m'mwamba kwambiri ngati mpheta, nkunda, mbalame ya ntundu wa mayina, atsekwe, ndi zina zambiri ndi zoyera. (*Durr-e-Mukhtār, Rad-dul-Muḥ tār, buku. 1, tsamba. 574; Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 113*)

Magazi a nsomba ndi woyera

Magazi a nyama zam'madzi kuphatikizapo nsomba komanso a nsikidzi ndi udzudzu ndi oyera. Chimodzimodzi, malovu ndi thukuta la miyulu komanso bulu ndi zoyera. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 114*)

Madontho ang'onoang'ono a nkodzo

1. Ngati madontho ang'onoang'ono ofanana ndi nsonga ya singano a nkodzo agwera pa thupi kapena chovala, thupi kapenanso chovala zonse zidzakhalabe zoyera. (*'Ālamgīrī, buku. 1, tsamba. 46; Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 114*)
2. Ngati mbali ya chovala chimene chili ndi madontho ngati amenewa chagwera m'madzi, madzi sadzakhala okuda kapena onyatsa nawonso.

² Mlame ndi mbalame imene imakonda mdima. Imangolendewera mozondoka m'mitengo, m'madenga ndi zina zambiri nthawi ya masana ndipo imawuluka usiku.

(Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 114)

Magazi otsalira mu nyama

Magazi otsalira mu nyama, chiwalo ndi chiwindi ndi oyera. Koma ngati zinthu zimenezi zadetsedwa ndi magazi oyenda ndiyeno zimakhala zosayera. Sizidzakhala zoyera mpakana zitatsukidwa. *(ibid)*

Mafupa owuma a nyama

Kupatula nkhumba, mafupa a nyama zina amene sanadetsedwe ndi mafuta a nyama yovunda ndi oyera. Ubweya komanso mano ake ndizoyeranso.

(Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 117)

Nkaka wa nyama za Ḥarām

Nkaka wa nyama za Ḥarām siwoyera. Komabe, nkaka wa kavalo wankazi ndi oyera, koma sizololedwa kumwa.

(Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 115)

Ndowe za mbewa

Ndowe za mbewa (ndi zosayera, koma ngati) zagayidwa pamodzi ndi tirigu kapena zagwera m'mafuta, ndiye ufa umenewu komanso mafuta zimakhala zoyera. Komabe, ngati kakomedwe kasintha ndiyeno ufa umenewu ndi mafutawo zimakhala zosayera. Ngati ndowe zimenezi zikupezeka pankate, chotsani gawo lozungulira ndowezo. Palibe vuto lililonse pakudya nkate wonse. *(Fatāwā 'Ālamgīrī, buku. 1, tsamba. 46, 48; Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 115)*

Ntchentche zopezeka pa nyatsi

1. Ngati ntchentche imene inali pa ndowe yawuluka ndipo yatera pa chovala, chovala sichidzakhala chodetsedwa.
(Bafār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 116)
2. Pokhapokha ngati zili zodziwika kuti matope a munjira ndiwosayera (mwina chifukwa cha nvula kapena chifukwa china), adzatengedwa ngati oyera. Choncho, ngati phazi kapena chovala chadetsedwa ndi matopewo ndipo Ṣalāh yapempheredwa opanda kuwatsuka matopewo, Ṣalāh idzakhala yatheka koma ndizabwino kwambiri kutsuka phazi lodetsedwa ndi matopewo komanso kupukuta chovala chodetsedwa ndi matopewo. *(ibid)*

Lamulo lokhuza madzi anvula

1. Madzi anvula okugwa kuchokera ku ngalande ya (denga) ndi oyera ngakhale patakhala nyatsi pa denga ponse kapena pakamwa pa ngalande kapenanso madzi amene akugwawo asakanikirana ndi nyatsi ndipo madziwo kuchuluka kwake ndi, ambiri kuposera kapena ochepa kuchepera theka [la nyatsi]. Ndi oyera pokhapokha ngati nyatsi yapangitsa kusintha kwa mbiri za madzi(monga mtundu, fungo kapena kakomedwe). Limeneli ndiye lamulo lolondola komanso lovomerezeka. Ndipo ngati nvula yasiya, kupangitsa kuyenda komanso kugwa kwa madzi kusiya, madzi ongoyima komanso madzi amene akugwa kuchokera pa denga adzakhala osayera.

(Bafār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 52)

2. Chimodzimodzi, madzi anvula amene akuyenda mungalande ndi oyer a pokhapokha ngati ntundu, fungo kapena kakomedwe ka zonyansa zikuwoneka m'madzimo. Pa nkhan i yopangira Wuḍū ndi madzi amenewa, ngati tinthu tating'onoting'ono tambiri ta nyatsi tikuyenda m'madzi moti mpakana tosachepera kamodzi kapena tambiri titha kupezeka m'madzi ngati madziwo atatengedwa ndi dzanja, ndiyeno madziwo adzakhala osayera pa nthawi imene madziwo atengedwa ndi dzanja, ndipo kupanga Wuḍū ndi madzi amenewa ndi Ḥarām, apo ayi amakhala oloedwa koma ndizabwino kuwapewa. (*ibid*)
3. Pambuyo pa nvula, ngati fungo, kakomedwe kapena tinthu tating'onoting'ono ta nyatsi zikupezeka m'madzi ongoyima a m'ngalande, ndiye madzi amakhala osayera, apo ayi amakhala oyer a. (*ibid*)

Madzi anvula ongoyima m'misewu

Madzi anvula ongoyima mu tinjira totsika komanso m'misewu ndi oyer a ngakhale mtundu wake utakhala wa matope. Nthawi zina amathanso kusakanikirana madzi a chimbudzi. Pamenepa, lamulo lomwe latchulidwa pamwambapa lidzagwira ntchito monga ngati pali Kusintha kwa ntundu, fungo kapena kakomedwe ka madzi chifukwa cha nyatsi, adzatengedwa ngati osayera, apo ayi amakhala oyer a. Komabe, pambuyo poti nvula yasiya, ngati madzi sakuyenda ndipo amayima pa malo amene ali ochepera bwalo la mapazi 225, ndipo nyatsi yochepa kapena tizidutswa ting'onoting'ono ta nyatsi tikuwoneka m'madzimo, pamenepa amakhala osayera. Chimodzimodzi,

ngati munthu wina wakodzera m'madzi, adzakhala osayera. Matope amene amawazika kumbuyo kwa mapajama kuchokera pa nthaka chifukwa cha kuyenda ndi oyera pokhapokha ngati zikudziwika kuti ali ndi nyatsi iliyonse.

Madontho a madzi owazidwa munsewu

Ngati madzi awazidwa mu msewu ndipo agwera pa chovala kuchokera pa nthaka, chovala sichidzakhala chodetsedwa, koma ndizabwino kwambiri kuchichapa. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 116*)

Thukuta lobwera pambuyo poziyeretsa ndi miyala

Ngati wina wapanga Istinjā (wayeretsa ziwalo zotulukira nkodzo ndi chimbudzi) pogwiritsa miyala pambuyo poti wapanga chimbudzi kapena wakodza ndipo thukuta lochokera ku chiwalo chimenecho chadetsa chovala kapena thupi; chovala chimenecho kapenanso thupilo zonse ziwiri sizidzakhala zodetsedwa. (*'Ālamgīrī, buku. 1, tsamba. 48; Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 117*)

Ngati galu wakhudza thupi la munthu

Ngati galu wakhudza thupi la munthu kapena chovala, thupi komanso chovala zonse ziwiri sizidzakhala zoyera ngakhale thupi la galu litakhala lonyowa. Komabe, ngati pa thupi la galulo pali china chake chimene chili chonyansa, lamulo lidzakhala losiyana. Komanso, ngati thupi komanso chovala zadetsedwa ndi malovu ake, zidzakhala zodetsedwa kapena kuti zosayera. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 117*)

Nanga ngati galu wayika mulomo mu ufa

Ngati nyama imene malovu ake ndi osayera ngati galu, (nkhumba, nkango, kambuku, nkhandwe, njovu, nyalugwe kapena nyama zina zolusa) zayika milomo yawo mu ufa, ndipo ufawo unali phala utakanyidwa, chotsani gawo limene nyama inanyambitayo, mbali yotsalayo ndi yoyera. Ndipo ngati ufa unali owuma, tayani mbali imene inanyowayo. *(Baf̣ār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 117)*

Nanga ngati galu wayika mulomo mu mphika

Ngati galu anayika mulomo mu mphika wadongo wogwiritsidwa ntchito umene uli osalala pamwamba kapena mphika wa dongo kapena wa chitsulo kapenanso mphika wadothi, udzakhala woyera pambuyo potsukidwa katatu; apo ayi udzakhala woyera pambuyo(potsukidwa komanso) kuwumitsidwa katatu. Komabe, ngati pali kung'ambika kofanana ndi tsitsi pa mphika owumbidwa kapena kusweka mu ziwiya zina ndiye pamenepa udzakhala woyera pambuyo potsukidwa komanso kuwumitsidwa katatu basi . Kungotsuka kokha sikudzayeretsa.

(Baf̣ār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 64)

Ngati galu wanyambita pamwamba kapena kuti panja pa mbiya, madzi amene ali m'menemo sadzakhala okuda. *(Baf̣ār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 64)*

Nanga ngati mphaka wayika mulomo m'madzi

Zotsalira (zinthu zimene zasiyidwa monga chakudya) za nyama zoweta monga mphaka, khoswe, njoka, buluzi ndi zina zambiri ndi 'Makrūf̣h'.

(Baf̣ār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 65)

Infa yonvetsa chisoni ya atsikana atatu

Nkaka, madzi ndi zakudya zina zikuyenera kuvundikiridwa. Iyi ndi nkhani yonvetsa chisoni imene inachitika ku Bāb-ul-Madīnaḥ Karachi.

Mwamuna ndi nkazi wake anasiya ana awo aakazi ang'onoang'ono atatu mu chisamaliro cha anthu oyandikana nawo kapena abale awo, ndipo anapita ku Hajj. Koma mwadzidzidzi, Hajj isanachitike, ana awo aakazi atatu onse anamwalira nthawi imodzi. Makolo olira anabwerera, akulira komanso kudandawula ku Bāb-ul-Madīnaḥ Karachi kuchokera ku Makkaḥ Kopatulika opanda kuchita Hajj. Pambuyo pofufuza, zinapezeka kuti nkaka unasiyidwa osavindikira; buluzi anagwera ndipo anafera momwemo. Ana aakazi ang'onoang'ono atatu aja anamwa nkaka omwewo ndipo poyizoni wake anapangitsa ngozi imeneyi. Zikunenedwa kuti ngati buluzi wafera mu chakumwa china chake ndipo waphulika, poizoni wake atha kupha anthu okwana 100.

Thukuta la nyama

Nyama yomwe zotsalira zake zimakhala zosayera, thukuta lake komanso malovu ake zimakhhalanso zosayera. Nyama yomwe zotsalira zake zimakhala zoyera, thukuta lake komanso malovu ake zimakhhalanso zoyera. Nyama yomwe zotsalira zake ndi Makrūḥ, thukuta lake komanso malovu ake amakhhalanso Makrūḥ.

(Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 66)

Thukuta la bulu ndi loyera

Ngati chovala chadetsedwa ndi thukuta la bulu kapena myulu, chovala chimakhala choyera, posatengera kuti thukuta ndi lochuluka bwanji.

(Bañār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 66)

Kumwa madzi ndi pamene kamwa ikutuluka magari

Ngati nkamwa mwa munthu mukutuluka magari kwambiri moti mpaka malovu ake asanduka ofiyira ndipo iye wamwa madzi nthawi yomweyo, ndiyeno madzi (otsalira) amenewa amakhala osayera. Ndipo pambuyo poti ntundu ofiyira wachoka, ndi zokakamizidwa kwa iye kuyeretsa nkamwa mwake potsukamo. Ngati iye sanatsuke nkamwa koma malovu adutsa pamwamba pa nyatsi kangapo kaya chifukwa cholavula kapena kumeza malovu, osasiyapo zizindikiro zilizonse za nyatsi, ndiyeno nkamwa mumakhala moyera ndithu. Ngati iye kenaka atamwa madzi, madziwo adzakhalabe oyera koma ndi zonyansa kwambiri komanso tchimo kumeza malovu munkhalidwe wotere (zikakhala ngati momwe zafotokozedweramu). *(Bañār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 63)*

Zotuluka ku chiwalo chankodzo cha munthu wamkazi

Zotuluka zimene zimatulutsidwa ndi chiwalo chankodzo cha akazi ndi zoyera. Ngati zadetsa thupi kapena chovala, sizoyenera kutsuka. Komabe, ndi zopambana kwambiri kutsuka. *(ibid, tsamba. 117)*

Nyama yovunda

Ngakhale sinyatsi, nyama yovunda komanso yotulutsa fungo ndi Ḥarām kudya . (*Baḥār-e-Sharī’ at, buku. 2, tsamba. 117*)

Botolo limene nkati mwake muli magari

Ngati munthu wapemphera Ṣalāḥ ndi botolo limene nkati mwake muli nkodzo kapena magari kapena mowa ndi zina zambiri m’thumba mwake, Ṣalāḥ yake imakhala sinatheke. Ngati muli dzira m’thumba mwake ndipo gawo limene limakhala la chikasu lasanduka kukhala magari, Ṣalāḥ idzakhala yatheka. (*ibid, tsamba. 114*)

Madzi ochokera nkamwa mwa Ntembo

Madzi otuluka kuchokera nkamwa mwa ntembo samakhala woyera kapena kuti amakhala odetsedwa. (*Fatāwā Razawīyyah (zatengedwa), buku. 1, tsamba. 268; Durr-e-Mukhtār, buku. 1, tsamba. 290*)

Zofunda zosayera

1. Ngati munthu wayika mapazi ake owuma pa nyatsi ndipo nthaka yonyowa yanyowetsa mapazi ake kapena pa nyatsi ndipo zofunda zonyowa zanyowetsa mapazi ake, ndiye mapazi ake adzakhalanso odetsedwa. Komabe, ngati pali chinyezi chabe (chinyezi ndi kuzizira zimene sizinganyowetse mapazi) ndiye mapazi sadzakhala odetsedwa. (*Baḥār-e-Sharī’ at, buku. 2, tsamba. 115*)

2. Ngati munthu wina wake akugona ndi zovala zosayera kapena pa zofunda zosayera ndiye zikupanga thukuta, ndipo zanyowetsa mbali yodetsedwa komanso thupi lake, thupi lidzakhala lodetsedwa apo ayi silidzadetsedwa. (*ibid, tsamba. 116*)

Mabuluku onyowa

Ngati chiwuno [gawo la mabuluku awiri amene miyendo imakumana pamwamba kapena kuti malo amene mbali ziwiri za mabuluku zimakumana] ndi chonyowa, ndipo iye watulutsa mpweya, chovala sichidzakhala chodetsedwa. (*ibid*)

Chidutswa cha khungu la munthu

Ngati khungu la munthu, ngakhale chofanana ndi kukula kwa chikhadabo, chagwera m'madzi ochepa (amene ali pamalo posakwana mapazi 225) madzi amenewo amakhala onyansa. Koma ngati chikhadabo chagwera m'madzi, madziwo sadzakhala onyansa. (*ibid*)

Ndowe zowuma

1. Kuphika chakudya pa ndowe zowuma zoyaka moto (za ng'ombe/njati) ndi zololedwa. (*Baḥār-e-Sharī' at, tsamba. 124, buku. 2*)
2. Ngati nkate walowetsa utsi wa ndowe yoyaka moto, nkate siwudzakhala onyansa. (*ibid, tsamba. 116*)

3. Phulusa la ndowe yowotchedwa ndi loyera koma ngati ndowe inathima isanasanduke phulusa ndiyeno pamenepa imakhala yosayera. (*ibid, tsamba. 118*)

Madzi onyansa amene agwera pa chophikira

Ngati madzi onyansa agwera pa chophikira kapena pa mbawula awuma chifukwa cha kutentha, nkate ophikidwa pamenepo siwumakhala onyansa. (*ibid, tsamba. 124*)

Tingayeretse bwanji nyama komanso chikopa cha nyama ya Ḥarām?

Kupatula nkhumba, nyama ndi chikopa cha chinyama chilichonse chimene chaphedwa ndi kuwerengedwa kwa بِسْمِ اللَّهِ chisanazingidwe ndi zoyera kaya chinyamacho ndi cha Ḥalāl kapena cha Ḥarām. Kutanthawuza kuti, ngati wina wake, amene akupemphera Ṣalāḥ, ali ndi nyama ya chinyama ngati chimenecho kapena wapemphera Ṣalāḥ pa chikopa cha chinyama chimenecho, Ṣalāḥ yake idzakhala yatheka. Komabe, nyama ya Ḥarām sidzakhala ya Ḥalāl kudya chifukwa choti yazingidwa. Idzakhala ya Ḥarām.

(*Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 124*)

Kukhalira pa chikopa cha mbuzi kumabweretsa kudzichepetsa

Munthu sakuyenera kukhala kapena kupempherera Ṣalāḥ pa chikopa cha nyama yolusa ngakhale chitawumitsidwa ndikusamalidwa bwino, chifukwa kutero kumusambitsa nkhanza ndi nkwiyo mu ntima. Kukhala pa chikopa cha mbuzi kapena nkhoa kapena kuvala kumabweretsa

kukoma ntima komanso kudzichepetsa mu ntima. Chikopa cha galu, kaya chawumitsidwa ngakhalenso galuyo atazingidwa, sichikuyenera kugwiritsidwa ntchito, chifukwa ndi bwino kupewa zinthu zimene ophunzira a Chisilamu ali ndi malingaliro osiyanasiyana kapena zinthu zimene anthu amanyatsidwa nazo. (*ibid, tsamba. 124-125*)

Zonyatsa zimene zimawoneka zimatchedwa ‘Mar-iyah’ ndipo zonyatsa zimene sizimawoneka zimatchedwa ‘Ghayr Mar-iyah’.

(*Bahār-e-Sharī’ at, buku. 2, tsamba. 54*)

Tingachape bwanji chovala chodetsedwa ndi nyatsi yolimba?

Ngati nyatsi ndi yolimba, imene imatchedwa ‘Najāsat-e-Mar-iyah’ (ngati chimbudzi, ndowe za chinyama, magari ndi zina zambiri.), ndiyeno kutsuka nyatsi kwa kanthawi si lamulo, komano kuchotsa nyatsi ndi zoyenera. Ngati nyatsi itachoka mu kuchapa koyamba, chidzakhala (chinthu chodetsedwa) chayera pambuyo poti chachapidwa kamodzi kokha. Ndipo ngati nyatsi yachoka pambuyo poti chinthu chodetsedwa chachapidwa kanayi kapena kasanu, ndiye kuchapa kanayi kapena kasanu ndikoyenera. Komabe, ngati nyatsi yachotsedwa mu kuchapa kochepera katatu, ndi Mustahab kumaliza katatu konse.

(*Bahār-e-Sharī’ at, buku. 2, tsamba. 119*)

Nanga ngati nyatsi yatsalira pa chovala?

Ngati nyatsi yachotsedwa koma zotsatira zina za nyatsi monga ngati ntundu kapena fungo zili pompo pa chovalapo

ndiyeno kuzichotsa zimenezo ndi zoyenera. Komabe, ngati zili zovuta kuchotsa zotsatira zake ndiyeno kuzichotsa sizoyenera. Motero, chovala chidzakhala choyera pambuyo pochichapa katatu. Kuchapa ndi sopo, asidi, madzi otentha (kapena makhwala) sizoyenera. (*Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 119*)

Ngale za Madanī 6 zoyeretsera chovala chimene chadetsedwa ndi nyatsi yo pepuka

1. Ngati nyatsi ili yo pepuka (ngati nkodzo ndi zina zambiri) ndiyeno chovala chidzayera pambuyo pochapa katatu ndipo mu katatu konse chifinyidwe ndi mphanvu zonse, mukunena kwina pasapezeke dontho la madzi likutuluka ngati chitafinyidwa kachikena. Ngati munthu sakufinya ndi mphanvu zake zonse poteteza chovala chake kuti chisawonongeke ndiyeno chovalacho sichidzakhala choyera. (*Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 120*)
2. Ngati munthu wochapa wachifinya ndi mphanvu zake zonse, kwa iyeyo ndi choyera. Komabe, ngati pali munthu wina amene ali wamphanvu kuposa munthu wochapa uja ndipo pali kuthekera koti dontho limodzi kapena madontho awiri a madzi atha kutuluka kuchokera mu chovala pamene chingafinyidwe ndi munthu wina uja (munthu wamphanvu kwambiri), ndi chosayera kwa munthu wachiwiri uja koma kwa munthu woyamba uja ndi choyera (munthu wochapa). Mphanvu za munthu wachiwiri uja sizidzakhala ndi zotsatira pa lamulo la munthu woyamba uja. Komabe, ngati munthu wachiwiri uja amachapa ndipo wafinya

chovala mofanana chimodzimodzi ndi munthu woyamba, chovala sichidzakhala choyera kwa munthu wachiwiri uja. (*ibid*)

3. Ndi zopambana kwambiri kutsuka manja pambuyo pofinya chovala ulendo woyamba komanso ulendo wachiwiri. Ndipo poti mwafinya ulendo wachitatu, ziwiri zonse chovala ndi manja zidzatengedwa ngati zoyera. Koma ngati chovala chili chonyowa kwambiri moti mpakana dontho limodzi kapena madontho awiri a madzi atha kutuluka kuchokera ku chovalacho ngati chitafinyidwa, ndiyeno pamenepa chovala komanso manja zonse zimakhala zosayera. (*ibid*)
4. Ngati munthu sanatsuke manja ake mu ulendo woyamba kapena ulendo wachiwiri, ndipo mbali ina yoyera ya chovala yanyowa ndi kunyowa kwa manja ake, mbali imeneyinso idzakhala yosayera pamenepa. Ngati mbali itanyowa pambuyo pakufinya koyamba, ndiyeno ikuyenera kuchapidwa kawiri, ndipo ngati itanyowa chifukwa cha kunyowa kwa manja pambuyo pakufinya kachiwiri, ndiyeno ikuyenera kuchapidwa kamodzi. Chimodzimodzi, ngati gawo la chovala choyera lanyowa chifukwa cha chovala chimene chinachapidwa komanso kufinyidwa kamodzi, ndiyeno liyenera kuchapidwa kawiri. Ndipo ngati lanyowetsedwa ndi chovala chochapidwa komanso kufinyidwa kawiri ndiyeno lidzayeretsedwa pochapidwa kamodzi basi. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 120*)
5. Ngati munthu wochapa wapachika chovala pa chingwe ndipo madontho ena a madzi akutuluka kuchokera mu

chovalacho pambuyo poti iye wachapa kale katatu komanso wafinya ndi mphanvu zake zonse mu ulendo uliwonse m'ma ulendo onse moti mpakana panalibe dontho lililonse linakatha kutuluka pa nthawi imene chafinyidwa kachikena, madzi otulukawa adzatengedwa ngati oyera pamenepa. Koma ngati iye sanafinye chovala ndi mphanvu zake zonse, ndiyeno madzi amenewa adzatengedwa kuti ndi osayera.

(ibid, tsamba. 121)

6. Sizoyenera kuchapa chovala katatu motsatizana. Ngati chachapidwa katatu mu nthawi zosiyana kapena ngakhalenso m'masiku osiyana, chovala chidzayerabe.
(ibid, tsamba. 122)

Kufinya silamulo pamene chovala chikuchapidwa pa mpope

Zafotokozedwa pa tsamba 35 la buku loyamba la *Fatāwā Amjadiyyah*: Lamulo (la kuchapa komanso kufinya chovala katatu) silidzagwira ntchito pamene chovala chikuchapidwa ndi madzi ochepa. Ngati chikuchapidwa pa dziwe lalikulu (limene likukwana pa malo a mapazi 225 kapena kuposera pamenepa, ngalande, mtsinje kapena nyanja ndi zina zambiri.) kapena madzi ambiri akuyenda (kuchokera mu mpope, payipi, kapena chotengera madzi³ ndi zina zambiri.) kumapita pa chovala kapena

³ Chotengera madzi ndi ntundu wakale wa chosungira chimagwiritsidwa ntchito kutungira madzi.

chikuchapidwa m'madzi oyenda (a mu mtsinje ndi zina.) ndiyeno kufinya silamulo mu zochitika zimenezi.

Kufinya silamulo pamene chovala chikuchapidwa pa madzi oyenda

Anthu odziwa malamulo a fiqh a Chisilamu رَحْمَهُمُ اللَّهُ anati: Ikani chovala chokhuthala, chiguduli kapena chovala china chilichonse chokuda pa madzi oyenda usiku wonse, chimasitha kukhala choyera. Chigamulo chenicheni ndi chakuti chovala chidzatengedwa kuti ndi choyera pamene pali kuthekera kwakukulu koti madzi akhoza kukokolola nyatsi chifukwa kufinya silamulo pa nkhani yoyeretsa chovala pa madzi oyenda. (*Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 121*)

Kuchapa zovala zoyera ndi zosayera pamodzi

Ngati chovala chimodzi chosayera chayikidwa m'madzi m'makina ochapira kapena ndowa pamodzi ndi zovala zoyera, pamenepa zovala zonse zidzakhala zosayera. Kupanga choncho popanda kupatulidwa kwa Shar'ī sizololedwanso. A'lā Ḥaḍrat, Imām-e-Aḥl-e-Sunnat, Maulānā Shāḥ Imām Aḥmad Razā Khān عَلَيْهِ رَحْمَةُ الرَّحْمَنِ anafotokoza pa tsamba 792 la buku loyamba la *Fatāwā Razawīyyah*: Kuchipanga chinthu choyera kuda kosafunikira ndi zosaloledwa komanso ndi tchimo. Iye اللَّهُ عَلَيْهِ رَحْمَةُ anafotokozanso pa tsamba 585, mu buku lachinayi: Popanda kufunikira kwa Shar'ī, kulipanga thupi kapena zovala kukhala zosayera ndi Ḥarām. Zafotokozedwa mu *Baḥr-ur-Rāiq*: 'Kuchipangitsa chinthu choyera kukhala chosayera ndi Ḥarām.'

(*Baḥr-ur-Rāiq, buku. 1, tsamba. 170*)

Choncho, alongo a Chisilamu ayenera kuchapa zovala zoyera ndi zosayera pazokhapazokha. Ngati akufuna kuchapa zonse pamodzi, ndiyeno iwo ayenera kuyeretsa mbali yodetsedwa ya chovala mosamala asanachape ndi zovala zina zakuda mu makina ochapira.

Njira yosavuta kuyeretsera zovala zokuda

Yotsatirayi ndi njira yosavuta yoyeretsera zovala: Ikani zovala zosayera mu ndowa ndipo tsegulani pa mwamba pake. Zipangeni zovala kumizidwa ndi thandizo la dzanja kapena ndodo ndi zina zambiri mwanjira yoti palibe gawo la chovala lililonse latsalira pa mwamba pa madzi. Pambuyo poti madzi ambiri achokamo mu ndowa ndipo munthu ali ndi chikhulupiro chachikulu kuti madzi achotsa nyatsi, ndiyeno zovala zimenezo ndi madzi mu ndowa, kuphatikizapo dzanja kapena ndodo zoviyikidwa m'madzi, zonse zidzatengedwa kuti ndi zoyera ngati palibe zizindikiro za nyatsi pa zovala ndi zinthu zina.

Pamene mukuyeretsa zovala mu njira imeneyi, tengani chisamaliro chofunikira kuti ngakhale dontho limodzi la madzi onyansa lisagwere pa thupi lanu kapena pa chinthu china chilichonse pokhapokha ngati muli chikhulupiro chachikulu. Ngati m'phepete kapena gawo lililonse la nkati mwa ndowa kapena chotungira madzi lanyowa ndi madzi onyansa; ndipo pansi siposalala komanso sipathyathyathya kuti madzi angayende kuchokera mbali zonse za m'phepete, kupangitsa m'phepete ndi malo ena kukhala osatsukidwa, ndiyeno pamenepa, gwiritsani ntchito kapu kapena dzanja lanu kupititsa pa madzi oyenda a mpope ndipo ayendetseni madziwo mbali iliyonse ya ndowa mwanjira yoti mpakana

m’phepete komanso mbali zina zosatsukidwa za nkati zatsukidwa komanso zayera. Komano pangani zimenezi kumayambiriro ndi cholinga choti musazipangenso zovala zanu zoyera kukhala zokuda!

Njira yoyeretsera zovala mu makina ochapira

Poyamba ikani zovala mu makina ochapira ndipo thiranimu madzi. Zipangeni zovala kumizidwa m’madzi ndi thandizo la dzanja lanu ndi zina zotero mwanjira yoti palibe gawo la chovala lotsalira kunja kwa madzi. Usiyeni mpope otsegula pa mwamba pa makina. Tsopano chotsani pulagi ya magetsi, chotsanimu madzi. Munjira imeneyi, madzi adzakhala akuchokera ku mpope ndipo adzakhala akutuluka kudzera mu ngalande. Pamene muli ndi chikhulupiriro chachikulu kuti madzi achotsa nyatsi, ndiyeno zovala komanso madzi mu makina zidzakhala zayera zonse, ngati palibe zizindikiro za nyatsi pa zovala. Ngati pali kufunikira, m’phepete mokhala m’mwamba mwa makina mukuyenera kutsukidwa kumayambiriro potsatira njira yafotokozedwa poyamba ija.

Njira yoyeretsera zovala pa mpope

Ndowa kapena mphika sinjira yokhayo yoyeretsera zovala m’njira yomwe tafotokozayi. Munthu athanso kuziyeretisa pozigwira pa mpope otuluka madzi. Mwachitsanzo, mpango wada. Ikani pa mpope ndipo madzi ayende pa mwamba pake mpakana ngati pali chikhulupiriro chachikulu kuti nyatsi yachoka. Mu njira imeneyi, chidzakhala chayera. Chovala chachikulu kapena gawo lake lokuda zithanso kuyeretsedwa mu njira yomweyi. Koma onetsani kuti madzi

onyatsa sanagwere pa thupi, zovala kapena malo ozungulira.

Kapeti yokuda ingayeretsedwe bwanji?

Chapani malo odetsedwa a kapeti ndipo pachikani; Ikhale chipachikire mpaka madontho a madzi atasiya kutuluka kuchokera mu kapetimo. Kenako, chapani ndi kupachika kachiwiri ndipo isiyeni ikhale chipachikire mpakana itasiya kutulutsa madzi. Kenako, chapani ndi kupachika kachitatu mu njira yomweyi, idzakhala yayera pamene yasiya kudontha madzi. Munthu atha kuyeretsa nkeka, nsapato-yachikopa ndi miphika yadongo ndi zina zambiri zimene zimalowetsa nyatsi yopepuka nkati mwake mu njira yake yomweyi. Nsalu yosalimba imene itha kung'ambika ngati itafinyidwa iyenera kuyeretsedwa mu njira yomweyi.

Njira ina yoyeretsera kapeti yokuda, chovala ndi zina zambiri ndi kumiza m'madzi oyenda (mwachitsanzo, mtsinje, mtsinje waung'ono, kapena pa mpope) ngati munthu ali chikhulupiriro chachikulu kuti nyatsi yachotsedwa ndi madzi. Ngati mwana wamng'ono wakodzera kapeti, pongowaza madontho ochepa a madzi pa kapetipo sizidzayeretsa kapetiyo. Kumbukirani, nkodzo wa khanda ngakhale longotha tsiku limodzi ndi osayera.

Tingayeretse bwanji manja amene apakidwa ndi henna onyatsa?

Ngati dzanja kapena chovala zadetsedwa ndi ntundu onyansa kapena henna onyansa, tsukani kapena kuchapa kochuluka mpakana madzi okugwa kuchokera m'manja ndi

oyera [opanda tinthu ta ntundu onyansa kapenanso henna nkati mwake]. Mu njira imeneyi, zidzakhala zayera ngakhale ntundu utakhalabe watsalira pa dzanja kapena pa chovala.

(Baĥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 119)

Kuchapa chovala chodetsedwa ndi mafuta

Ngati chovala kapena thupi zadetsedwa ndi mafuta onyansa, zidzayera pambuyo pochapa kapena kutsuka katatu ngakhale mafuta atsalirabe. Sizoyenera kuchapa ndi sopo kapena madzi otentha. Koma ngati zadetsedwa ndi mafuta a nyama yovunda, sizidzayera pokhapokha mafuta atachotsedwa.

(Baĥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 120)

Ngati gawo lochepa la chovala lakhala lokuda...

Ngati gawo la chovala lakhala lokuda komano sizikudziwika kuti gawo lake liti, ndiyeno ndi zabwino kwambiri kuchapa chovala chonse (lamulo ili lidzagwira ntchito pamene gawo losayera silikudziwikiratu. Ngati likudziwika, mwachitsanzo, dzanja la chovala lakhala lokuda komano sizikudziwika kuti ndi gawo lake liti la dzanja la chovala limene lakhala lokuda, ndiyeno kuchapa dzanja lonse la chovala kudzatengedwa ngati kuchapa chovala chonse). Ngati munthu wachapa gawo lililonse la dzanja la chovala pambuyo poti iyeyo waganizira, ndiyeno chidzakhhalanso chayera. Ngati wina wachapa gawo lililonse mopanga kuganizira ndiyeno pamenepanso chidzakhala chayera. Koma ngati atazindikira pambuyo poti atapemphera Ṣalāḥ zingapo kuti gawo losayera silinachapidwe, iye ayenera kuchapa kachikena komanso kubwerezanso Ṣalāḥ zonse

(kuzipemphera kachikena). Komabe, ngati kulakwika kwawoneka mu nkhani yoyamba ija m'mene kuganizira kunachitika, iye ayenera kuchapa panopa komano kubwereza Ṣalāh zimenezo sizofunika.

(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 121-122)

Kulibwanji kuchapa chovala ndi nkaka?

Chovala chochapidwa ndi nkaka, msuzi kapena mafuta sichidzayera chifukwa nyatsi sizingachotsedwe ndi zinthu zimenezi.

(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 119)

Malamulo 6 a kuyeretsa zovala zimene zadetsedwa ndi umuna

1. Ngati gawo lodetsedwa ndi umuna la chovala lawuma, chidzakhala chayera chovalacho pambuyo poti umuna wapukutidwa komanso wachotsedwa, ndipo chovalacho chakupulidwa. Ngakhale patakhala kuti pa chovala pali zotsatira zina pambuyo popukuta, chidzatengedwa ngati chayera. *(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 122)*
2. Pamenepa, lamulo lomweli latchulidwa m'mwambamu lidzagwira ntchito kaya umuna ndi wa mamuna kapena mkazi kapena munthu kapena nyama kapena wa munthu wa thanzi kapena wodwala wa Jiryān⁴. *(Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 122)*

⁴ Jiryān ndi matenda omwe umuna umatuluka Kaya pamodzi ndi nkodzo kapena nkodzo usanatuluke kapena pambuyo pa nkodzo.

3. Ngati thupi ladetsedwa ndi umuna, gawo la thupi lidzayeretsedwa mu njira yake yomweyi. (*ibid*)
4. Pambuyo pokodza, ngati munthu sanapeze kuyera popanga istinjah – kaya ndi madzi kaya miyala – ndipo umuna wayenda pamwamba pa mwamba pa malo odetsedwa ndi nkodzo, ndiyeno sipadzayeretsedwa posisita. M'malo mwake akuyenera kutsukidwa pamenepapa. Ndipo ngati munthu wadziyeretsa popanga istinjah kapena umuna watuluka mopanda kugundana ndi malo odetsedwa aja, ndiyeno kuyera kutha kupezedwa popukuta komanso kuchotsa umuna. (*ibid, tsamba. 123*)
5. Chovala chimene chayeretsedwa popukuta sichidzakhala chakuda ngati chitanyowa pambuyo poti chayeretsedwa kale. (*ibid*)
6. Ngati umuna wadetsa chovala ndipo ndichonyowabe, ndiyeno chitha kuyeretsedwa pochapa. Kupukuta umuna (usanawume) sizidzakhala zokwanira. (*ibid*)

Ndi nthawi yake iti imene ndi Wājib kumuwuza munthu zokhudza zovala zake kuti ndi zakuda?

Ngati munthu wawona nyatsi pa chovala cha Msilamu, ndipo pali kuthekera kwakukulu kuti ngati atamudziwitsa zokhudza nyatsiyo, iye ayiyeretsa ndiyeno kumuwuza ndi Wājib. (Pamenepa, munthu adzakhala ochimwa ngati sanamudziwitse.) (*Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 127*)

Njira yoyeretsera ubweya wa thonje

Ngati thonje lambiri ndi losayera munga momwe likuyembekezeka kuwuluka, malingana ndi chikhulupiriro chachikulu cha munthu, pa nthawi ya ndondomeko yoyika thonje pamodzi, ndiyeno thonje lidzakhala layera pamene layikidwa malo amodzi. Apo ayi, silidzakhala loyera pokhapokha litachapidwa. Komabe, ngati zikudziwika kuti ndi thonje lochuluka bwanji limene lili losayera, lidzakhala loyera pamene ndondomeko yoyika pamodzi yachitika. *(Bafār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 125)*

Njira yoyeretsera miphika

Ngati zinthu zimene sizingalowetse nyatsi nkati mwake zakhala zodetsedwa munga miphika yachi china, miphika ya ndongo yogwiritsidwa ntchito yokhala ndi pamwamba posalala kapena zinthu zopangidwa ndi zitsulo, nkuwa kapena ntundu wina wa nkuwa ndi zina zambiri, ndiyeno kungozitsuka zinthu zimenezi katatu ndi zokwanira (kuyeretsa). Sizofunikira kuzipachika kapena kuziyanika mpakana madzi atasiya kudontha.

(Bafār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 121)

Njira yoyeretsera mpeni ndi zina zambiri

Ngati chinthu chopangidwa ndi chitsulo munga mpeni, lupanga, lupanga lalitali ndi zina zambiri sizinachite dzimbiri ndipo zilibe zosema zakhala zodetsedwa, zidzayeretsedwa pamene zapukutidwa bwinobwino. Pamenepa, zilibe kanthu Kaya nyatsi yolimba kapena yopepuka. Chimodzimodzi, ngati zithu zopangidwa ndi siliva, golide, mkuwa, chokutidwa ndi golide kapena chitsulo chilichonse chopanda zosema,

zimayera pamene zapukutidwa. Ndiye ngati zili ndi zosema kapena zili ndi dzimbiri, zikuyenera kutsukidwa. Sizidzayeretsedwa pongopukuta chabe. (*Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 122*)

Njira yoyeretsera galasi

- Ngati galasi komanso chilichonse chopangidwa ndi galasi, miphika yachi china kapena mphika wadongo opakidwa zinthu (kapena mphika wadongo wonyezimira ndi galasi lopyapyala) kapena matabwa opukutidwa ndi zinthu zina zake, mwachidule, chinthu chilichonse chimene chilibe mabowo chakhala chodetsedwa, zidzayera pamene zapukutidwa ndi nsalu/chovala kapena tsamba kufikira mpakana zotsatira za nyatsi zitachoka zonse pamodzi. (*Baḥār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 122*)

Koma, Kumbukirani! Ngati pali kusweka kapena gawo lina lake lachoka kapena chawonongeka kapena zinthu zagwiritsidwa ntchito zachoka pa malo ena – mwachidule, ngati pali kulimba kulikonse, kungopukuta mbali imeneyo sikudzakhala kokwanira, m'malo mwake kuyeretisa zinthu zimenezi pochapa ndi zoyenerera.

Njira yoyeretsera nsapato

Ngati masokosi (opangidwa ndi chikopa) kapena nsapato zadetsedwa ndi nyatsi yolimba ngati ndowe za munthu, ndowe za chinyama kapena umuna, zidzayeretsedwa pamene zapukutidwa komanso kuchotsedwa ngakhale nyatsi itakhala kuti ndiyonyowabe. Ngati (zinthu) zimenezi

zadetsedwa ndi madzi onyansa monga nkodzo, ndiyeno ikani dothi, phulusa kapena mchenga pa nyatsi ndipo zipukuteni, zidzakhala zoyera. Ngati munthu sanapange zimenezi ndipo nyatsi yawuma, ndiyeno sizidzakhala zoyera opanda kuzichapa. (*Bahār-e-Sharī' at, buku. 2, tsamba. 123*)

Majuzi ogwiritsidwa ntchito ndi zina zambiri za anthu oti si-Asilamu

Majuz, masokosi, makapeti komanso zovala zogwiritsidwa ntchito kale zochokera mayiko omwe si-Aasilamu zimatengedwa kuti ndi zoyera pokhapokha zizindikiro za nyatsi zikuwoneka. Kupemphera Ṣalāh mu zovala zimenezi opanda kuzichapa ndi zololedwa. Komabe, ndi zabwino kwambiri kuziyeretsa. Pa tsamba 127 la *Bahār-e-Sharī'at*, buku 2 (losindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madīnaḥ), Ṣadr-ush-Sharī'ah, Badr-uṭ-Ṭarīqah, 'Allāmah Maulānā Muftī Muhammad Amjad 'Alī A'zamī عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْقَوِي anafotokoza kuti: Zovala zogwiritsidwa kale ntchito za anthu ophwanya malamulo zidzatengedwa kuti ndi zoyera pokhapokha ndi zodziwika kuti ndi zosayera komano ndi pofunika kwa munthu amene amapemphera Ṣalāh kuyeretsa chiwuno cha mabuluku kapena kuti malo amene mabuluku amalumikizidwa chifukwa munthu amene samapemphera Ṣalāh nthawi kawirikawiri amavala mabuluku akangomaliza kukodza opanda kuziyeretsa popanga istinjah. Chisamaliro chachikulu chiyenera kutengedwa pa nkhani yovala zovala zogwiritsidwa ntchito kale za anthu amene si-Aasilamu. (*Bahār-e-Sharī' at, gawo 2, tsamba. 127*)

صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

pambuyo poti mwawerenga kabukuka, mutha kukhala ndi chikhumbokhumbo chodziwa amene analemba. Choncho mverani! Kabukuka kanalembedwa ndi Wankulu wachipembedzo ndi maphunziro wowunikira mu zaka za zana la 21, ‘Allāmah Maulānā Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَةِ. Iye anayambitsa **Dawat-e-Islami** (bungwe lapadziko lonse komanso silandale lolalikira Quran ndi Sunnah) limene likufalitsa maphunziro a Chisilamu m’magawo oposa 93 a umoyo. Ngati mukufuna kudziwa zokhudza Myambitsi wa Dawat-e-Islami, mabuku ake, timabuku, komanso nthambi zosiyanasiyana za Dawat-e-Islami, pitani pa webusayiti iyi: www.dawateislami.net Komanso, Dawat-e-Islami ikufalitsa uthenga wa Chisilamu dziko lonse lapansi kudzera pa kanema wawayilesi otchedwa **Madani Channel**, wayilesi ya kanema imene zinthu zake zimakhala ma 100 peresenti za chisilamu. Posatengera komwe muli m’dziko lapansi, ngati mukufuna kuwonera Madani Channel, ndiye tsatirani ma frequency aperekedwawa. Ngati mukufuna kulumikizana nafe, ndiye titumizireni imelo pa keyala iyi : overseas@dawateislami.net

Madani Channel – Satellite Frequencies

Modulation: QPSK

Satellite	Coverage	Downlink Frequency	Symbol Rate	Polarization	FE C
Asia sat 3S	Asia	3739 MHz	2815 Msps	Vertical	3/4
Astra 2F	UK	12640 MHz	22000 Msps	Vertical	5/6
Intelsat 20	Africa Region	12562 MHz	26657 Msps	Horizontal	2/3

Eutelsat 7 West A	Middle East Region	10815 MHz	27500 Msps	Horizontal	5/ 6
Galaxy 19	USA Region	11960 MHz	22000 Msps	Vertical	3/ 4

KUPHUKA KWA MA SUNNAH

Mwa chisomo cha Allah, maSunnah (njira zotsatira za Mtumiki) amaphunzitsidwa komanso kuphunzirikidwa mochuluka mu chikhaliidwe cha 'Madani' cha Dawat-e-Islami, gulu lapadziiko lonse komanso losachita ndale lophunzitsa Quran komanso Sunnah. Ndi pempho la Madani kuti mukhale usiku wonse mu 'Ijtima' (msonkhano) wolimbikitsa Sunnah ya sabata iliyonse, yomwe imachitika pambuyo pa 'Salat-ul-Maghrib' Lachinayi lililonse mu nzinda wanu, chifuika chofuna kusangalatsa Allah ndi zolinga zabwino. Ndi cholinga chofuna kupeza mphotho, chikhale chizolowezi chanu kuyenda mu 'Madani Qafilah' (magulu oyenda) olimbikitsa Sunnah, ndi okonda Rasul (Mtumiki), kulemba nkabuku konse ka 'Madani In'amat' tsiku lililonse mukuchita 'Fikr-e-Madinah' (kuganizira za Madinah) ndikupereka kwa m'bale wa Chisilamu woyenera wa dera lanu nikati mwa masiku khumi oyambirira a mwezi uliwonse wa Chisilamu. Kudzera mu madalitso a izi, mudrakulitsa malingaliro ndi chilakolako chokhazikitsa MaSunnah, kukhala ndi chidani cha machimo ndikuteteza chikhulupiro chanu

M'bale aliyense wa Chisilamu ayenera kukulitsa malingaliro a Madani akuti Ndiyenera koyesetsa kudzikonza ndekha ndi anthu a dziko lonse lapansi, **بذلک الله یهدی الیک صراطاً مستقیماً**. Kuti tidzikonze tokha, tiyenera kuchita malinga ndi Madani In'amat ndikuyesetsa kukonza anthu a dziko lonse lapansi, tiyenera kuyenda ndi ma Madani Qafilah, **یومئذ یخرجون فی قافلات**.



ISBN 978-969-631-261-1



0109520

**MAKTABATUL
ADINAH**

Asim Madani Markaz, Faiz-e-Madinah, Mahallat Sandagan
Parasi Sahi Mundi, Bah-ul-Madinah, Karachi, Pakistan
UAN: +92 21 111 25 26 92 Ext: 1262

E-mail: translation@dawateislami.net Web: www.dawateislami.net